



YESU SANADE NKHAWA

Yolembedwa ndi Tony Alamo

2 Akorinto 1:4-14 akuuza aliyense amene akumuwerenga kuti MULUNGU wa a Khristu ndi MULUNGU “Wotitonthoza ife m’masautso athu onse, kuti tidzathe ife kutonthoza iwo okhala m’masautso ali onse, mwa chitonthozo chimene titonthozedwa nacho tokha ndi MULUNGU. Pakuti monga masautso a KHRISTU atichulukira ife, choteronso chitonthozo chathu chichuluka mwa KHRISTU. Koma ngati tisautsidwa,

kuli chifukwa cha chitonthozo ndi chipulumutso chanu, chimene chichitsa mwa kupilira kwa masautso omwe wo amene ifenso timva: kapena ngati titonthozedwa, kuli kwa chitonthozo ndi chipulumutso chanu. Ndipo chiyembekezo chathu cha kwa inu ndi chokhankikika, podziwa, kuti monga muli oyanjana ndi masautsowo, koteronso chikhale cha chitonthozo.

“Pakuti sitifuna, abale, kuti mukhale osadziwa za chisautso chathu tinakomana nacho ku Asia, kuti tinathodwa kwakukulu, koposa mphamvu yathu, kotero kuti tinada nkhawa ngakhale za moyo wathu: Koma tinakhala nacho chitsutso cha imfa mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa MULUNGU wakuukitsa akufa: Amene anatilanditsa mu imfa yayikulu yotere,

nadzalanditsa: amene timuyembekezera kuti IYE adzalanditsanso; Inunso pothandizana ndi pemphero lanu la kwa ife, kuti pa mphatso ya kwa ife yodzera kwa anthu ambiri payamikike ndi anthu ambiri chifukwa cha ife.

“Pakuti kudzitamandira kwathu ndiko, umboni wa chikumbumtima chathu, kuti m’chiyero ndi kuna mtima kwa Mulungu, osati ndi nzeru ya thupi, koma m’chisomo cha MULUNGU takhala tikukambirana m’dziko lapansi, makamaka kwa inu. Pakuti sitilemba kwa inu zina, koma zimene muwerenga kapenanso muvomereza; ndipo ndiyembekeza kuti mudzavomereza kufikira chimaliziro; Monganso munativomerezera ife pena, kuti ife ndife kudzitamandira kwanu, monga momwe inunso muli

kudzitamandira kwathu m’tsiku la AMBUYE YESU.”

YESU akudziwa mathero a chili chonse.¹ Pamene IYE anakwera m’ngalawa ndi ophunzira AKE, IYE anadziwa kuti kukhala mphepo ya mkutho, namondwe wamphamvu, IYE asanakagone kumbuyo kwa ngalawa. Mawu a m’chi Giriki akuti namondwe anali wamkulu panyanja kotero kuti ngalawa inafundidwa ndi mafunde kufuna kumila. YESU sanade nkhawa! Matenda ambiri amayamba chifukwa cha nkhawa ndipo imapanigitsa mamiliyoni a anthu kukhala ali pa mankhwala ambirimбири. Ophunzira anali ndi nzeru zokwanira kupita kwa YESU m’pemphero. “AMBUYE, tipulumutseni: [tisana] tayike” (Mat-

(Yapitirira patsamba 2)

YESU SANADE NKHAWA

(Yachokera patsamba 1)

eyu 8:25). YESU anangodzudzula nyanja ndi mphepo, ndipo panagwa bata lalikulu (Mateyu 8:26).

Lazaro anali nkudwala ndipo anamwalira. YESU sanade nkhwawa. Pamene Yesu anamva za kudwala kwa Lazaro (ndi kudziwa za imfa yake), IYE anakhala masiku ena awiri pa malo pomwepo pamene IYE amakhala. Kenako IYE anauza ophunzira AKE, “tiyeni tipitenso ku Yudeya.” Ophunzira AKE anamukumbutsa IYE (anaganiza), “Ayuda analikufuna kukuponyani INU miyala tsopano apa; ndipo INU munkanso komweko kodi?” YESU sanade nkhwawa. “YESU anayankha, Kodi sikuli maola khumi ndi awiri usana? Ngati munthu ayenda usana, iye sakhumudwa [ngati munthu ayenda mwa MZIMU WOYERA, iye sakhumudwa, chifukwa akutha kuona kumene MULUNGU akumutengera], chifukwa apenya kuunika kwa dziko lino lapansi. Koma ngati munthu ayenda usiku [opanda MZIMU wa MULUNGU kumutsogolera], iye akhumudwa, chifukwa mulibe kuunika mwa iye [Anthu amenewa amakhala ndi nkhwawa nthawi zonse!].

“Zinthu izi anati IYE: ndipo zitatha izi IYE ananena nawo, Lazaro bwenzi lathu ali m'tulo; koma ndimuka, kukamuukitsa iye tulo take. Ndipo ophunzira AKE anati, AMBUYE, ngati ali m'tulo, adzachira. Koma Yesu anali kunena za imfa yake: koma iwowa anayesa kuti IYE anali kunena za mpumulo wa tulo. Pamenepo Yesu anati kwa iwo momveka, Lazaro wamwalira. [YESU sanade nkhwawa. Nkhawa zichitanji koposa kuyambitsa matenda? IYE anali kudziwitsa ophunzira AKE kuti IYE anali kudziwa tsogolo, monga IYE

adziwa za pano ndi za m'mbuyo.² IYE anati,] Ndipo ndikondwera chifukwa cha inu kuti kunalibe INE komweko, chakuti mukakhulupire [Mu MAWU AKE ndi kuthekera KWAKE kokwanitsa kuchita zonse (zabwino) ndi kudziwa chili chonse]; koma tiyeni tipite kwa iye” (Yohane 11:1-15).

“Ndipo Marita anati kwa YESU, AMBUYE, mukadakhala INU munali kuno, mlongo wanga sakadafa. Koma ngakhale tsopano, ndidziwa, kuti zinthu zili zonse INU mukapempha MULUNGU, adzakupatsani INU MULUNGU. YESU ananena naye, Mlongo wako adzauka. Marita ananena ndi IYE, Ndidziwa kuti adzauka m'kuuka tsiku lomariza. Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuukanso, moyo: wokhulupilira INE, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo: Ndipo yense wakukhala ndi moyo nakhulupilira INE sadzamwalira nthawi yonse. Kodi mukhulupilira ichi? Ananena ndi IYE, inde, AMBUYE: ndakhulupilira ine kuti INU ndinu KHRISTU, MWANA wa MULUNGU, wakudza m'dziko lapansi.

“Ndipo mmene anati ichi, anachoka, nayitana Mariya m'bale wake mseri, ndikuti, Wafika MPHUNZITSI, ndipo akuyitana iwe. Koma iyeyo, pakumva, ananyamuka msanga, nadza kwa IYE. Koma YESU sanafike kumudzi, koma anali pamalo pomwe Marita anakomana ndi Iye. Pamenepo Ayuda okhala naye m'nyumba, ndikumutonthoza iye, pakuona Mariya, kuti ananyamuka msanga natuluka, anamtsata iye, nati, amuka kumanda kukalira komweko.

“Pomwepo Mariya pofika pamene panali YESU, mmene anamuona IYE, anagwa pa mapazi AKE, nanena ndi IYE, AMBUYE, mukadakhala kuno INU, mlongo wanga sakadamwalira. Pamenepo YESU pakumuona iye ali kulira, ndi Ayuda akumperekeza iye ali kulira, IYE anadzima mu MZIMU, navutika, nati, mwamuika iye kuti? Ananena ndi IYE, AMBUYE, tiyeni

mukaone. YESU analira. Ndipo Ayuda ananena, taonani momwe IYE anankondera! Koma ena mwa iwo anati, kodi UYU, wotsegula maso osaona, sanakhonza kodi kuchita kuti sakadafa ameneyunso? Pamenepo YESU ndikudzumanso mwa IYE YEKHA anadza kumanda. Koma panali mphanga, ndipo mwala unayikidwa pamenepo.

“YESU ananena, chotsani mwala. Marita, mlongo wake wa womwalirayo, ananena ndi IYE, AMBUYE, anayamba kununkha: pakuti wagona masiku anayi. YESU ananena naye, Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati ukhulupilira, udzaona ulemelero wa MULUNGU? Pomwepo anachotsa mwala pamalo pamene anamuyika womwalirayo.

“Koma YESU anakwenza maso AKE kupenya Kumwamba nati, ATATE, ndikuyamika INU kuti INU munamva ine. Ndipo ndidziwa INE kuti mumandimva INE nthawi zonse: koma chifukwa cha khamu la anthu layima ndinanena ichi, kuti akhulupire kuti INU munandituma INE. Ndipo mmene IYE ananena izi, IYE anafuula ndi mawu akulu, Lazaro, tuluka. Ndipo womwalirayo anatuluka, womangidwa miyendo ndi manja ndi nsalu za kumanda: ndi nkhope yake inazingidwa ndi mlezo. YESU ananena nawo, M'amasuleni iye, ndipo mlekeni amuke. Chifukwa chake ambiri mwa Ayuda amene anadza kwa Mariya, mmene anaona chimene YESU anachita, anakhulupilira IYE” (Yohane 11:21-45).

YESU yemweyi anati, ngati mukhulupilira, inu mudzapulumutsidwa.³
(Yapitirira patsamba 4)

³ Marko 16:16, Yoh. 3:17-18, 6:28-29, 40, Mac. 16:31, Aro. 10:9, 1 Tim. 1:16, Ahe. 3:12-14, 1 Yoh. 3:22-23, 5:12-13



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI
www.alamoministries.com

MAKALATA OPITA KWA M'BUSA ALAMO

Pakistan

Ndizomvetsa chisomo kwambiri kuti a Khristu ambiri akuzunzidwa chifukwa chakukhulupi-lira chi Khristu. Ku Pakistan a Khristu ambiri akukumana ndi zowawa ndikugwira ukaidi chi-fukwa chakukhala m'Khristu. Koma zinalembedwa mu Baibulo, "Odala muli inu, mmene ad-zanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa zili zonse chifukwa cha Ine." Ndinapita khomo ndi khomo kugawa zolembedwa. Ndinalingiza anthu za zolembedwa ndiku-nena kuti, "Zolembedwa izi ndizothandiza kwambiri kulimbikitsa moyo wathu auzimu, tiziziwe-renga." Ndapemphanso anthu kuti azipemphelera a Khristu amene akukumana ndi mayesero okhoma chifukwa chokhala m'Khristu. Chonde pempherani kuti Mulungu awamasule ku vuto lili lonse ndi kuwateteza nthawi zonse.

D.J.

Punjab, Pakistan



D.J. kugawa zolembedwa za Uthenga Wabwino wa M'busa Alamo m'mizinda ya Punjab, Pakistan

Oklahoma

Wodzodzedwa munthu wa Mulungu, M'busa Tony Alamo:

Muli odalitsidwa chifukwa Mulungu wakusankhani inu, m'busa weniweni wa dziko lonse, kudzalalika uthenga wabwino wa Yesu Khristu ku ngodya zinayi za dziko lino lapansi. M'zaka zambiri zonsezi, munanyamula mtanda wa Khristu, mwapilira nkondo yaikulu ya zowawa, mazunzo osatha, ndi mnyozo waukulu zedi komanso kupanikizidwa ndi mabodza ndiponso zidzudzulo. Yesu anati mu Yohane 15:18, "Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwa kuti linada Ine lisanayambe kuda inu." Yohane 15:19, "Mukadakhala a dziko lapansi, dziko lapansi likadakonda zake za lokha: koma popeza simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, chifukwa cha ichi likudani inu." Yohane 15:21, "Koma izi zonse adzakuchitirani chifukwa [cha Khristu], chifukwa sadziwa lye wondituma Ine...[yemwe ali Mulungu]." Mateyu 5:11, "Wodala muli inu, mmene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani zonama zoipa zili zonse, chifukwa cha Ine."

Tili wokondwa kukhala gawo la Tony Alamo Christian Ministries, pakuti tadalitsika m'madalitso auzimu onse mwa Khristu Yesu chifukwa ndi kuno kumene timaphunzira Mawu a Mulungu opanda kuweruzana. Yeremiya 3:15, "Ndipo ndidzakupatsani inu Abusa monga mwa mtima Wangwa, amene adzakudyetsani inu nzeru ndi luntha." Mitima yathu ili nanu, M'busa Alamo, pakuti Ambuye Khristu kudzera mwa inu walimbitsa dziko lino lapansi kufika penipeni, ndi uthenga wabwino wamatamando a Khristu, ndi mauthenga amene mumabweretsa ndi kutumiza ku dziko lonse lapansi kukafikira anthu onse pa dziko lonse lapansi amene amva ludzu lakufuna kumwa Mawu a Mulungu.

Mawu sangathe kufotokoza mmene ndakhala pano kukulemberani kalata iyi mwakukhulupilira kuti mwa njira ina ikukhudzani monga mwakhala kwambiri mukukhudza mahandredi ama sauzande ngakhalenso mamiliyoni ndi mphatso imene Mulungu anakupatsani ndipo momasuka mumayipereka kwa aliyense. Tikukuthokozani,

M'busa Alamo, pamene mukupitiriza kupempherera ndi kulangiza molimbika anthu a Mulungu ndi iwo a dziko lino lapansi amene akhulupilira zoonadi zosakanika za Mulungu. Muli m'mapemphero athu nthawi zonse ndi m'mitima yathu pamene tidza pamaso pa mpando wa chifumu wa Mulungu mu Mzimu umodzi ndi mu umodzi wa thupi la Khristu, monga Petro anamasulidwa ku ndende ndi mngelo wa Mulungu, ndiponso Paulo ndi Sailasi anaimba nyimbo zotamanda kwa Mulungu ndipo chivomerezi chachikulu chinadza mwadzidzi, kotero kuti maziko a ndende anagwedezeka, pomwepo makomo onse anatseguka (Machitidwe 12:5-9 ndi Machitidwe 16:25-26). Ulemelero kwa Mulungu pamene tikudikilira modekha kuona zodabwitsa zazikulu m'mene Mulungu adzakwaniritse malonjezo kwa inu ndi anthu Ake. Timakukondani M'busa Alamo, Mulungu akulimbikitseni ndi kupitiriza ntchito Zake zopambana mwa inu monga tidziwa lye adzatero. Wanu mwa Khristu,

Frankie Perez

Roland, OK

YESU SANADE NKHAWA

(Yachokera patsamba 2)

Muyitaneni IYE tsopano ndi pemphero ili ndipo mudzapulumutsidwa:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.⁴ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.⁵ Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wantengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.⁶ Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,⁷ ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.⁸ Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.⁹ Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wantengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.¹⁰ Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali

AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.¹¹ MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.¹² Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.¹³ Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.¹⁴

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.¹⁵ Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.¹⁶

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa

ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumbibera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale lenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, waterno AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

4 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 5 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 6 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 7 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 8 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 9 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 10 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 11 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 12 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 13 Aheb. 11:6 14 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 15 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 16 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereeni.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078
Twenty-four hour prayer and information line: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362
www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha. Chonde imbani +1 (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.

Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1 (661) 252-5686.

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).
MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:

© Copyright February 2011, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered February 2011, 2015

CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 12600—JESUS NEVER WORRIED